# MALAWI ELECTORAL COMMISSION

**Lonjezo La Atsogoleri a Zipani Zandale pa mmene achitire m'nthawi yokopa anthu kuti awasankhe**

*Ife* atsogoleri a zipani zandale moimilira onse amene akupikisana nawo pa zisankho;

*pozindikira* kuti dziko la Malawi limapatsa ufulu wandale;

*motsogozedwa* ndi lamulo lomwe limafotokoza za mmene chisankho chiyendetsedwere komanso mmene misonkhano yokopa wanthu ingachitikire;

*ndi khumbo* lofuna kugwirizana ndi bungwe loyendetsa zisankho kuonetsetsa kuti chisankho chachitika mwa bata ndi mtendere komanso movomerezeka;

Tsopano tikulonjeza kuti munthawi yopangisa misonkhano yokopa anthu ife tikuzindikira kuti:

1. m'nyengo yokopera anthu kuti ativotere ndi miyezi iwiri ndipo idzatha patatsala masiku awiri kuti anthu ayambe kuponya voti,

2. zipani zonse zandale komanso anthu onse omwe akupikisana nawo pa zisankho ali ndi ufulu ochititsa misonkhano yokopa anthu kuti adzawavotere mmalo ena alionse ovoemerezeka ndi malamulo mdziko muno;

3. chipani china chiri chonse chandale, aliyense amene akupikisana nawo pa zisankho komanso owaimilira kapena owatsatira ali ndiufulu woyankhula zakukhosi mosayang'anira kapena kuopa wina aliyense komanso ali ndi ufulu wochititsa misonkhano yokopa anthu mwamtendere mosaopsezedwa ndipo ife tidzapewa mchitidwe wa ziwawa komanso tidzaneneza aliyense wochita za chiwawa, woopseza anzawo ndi awo osalolerana;

4. ife sitidzayankhula mau onyoza anthu ena kapena kutukwana ena kapenanso kugwiritsa ntchito mau omwe angathe kuyambitsa chisokonezo kapena chifwilimbwiti;

5. tiri ndi udindo odziwitsa abwana DC za malingiliro ndi chilinganizo chofuna kupangitsa msonkhano wokopa anthu powalembera kalata yomwenso tidzipereka kwa wamkulu woyang'anira a police m'bomalo;

6. pali malo ena omwe ndiwosavomerezedwa kuti tingathe kukapangirako misonkhano yokopa anthu ndipo ife tiri ndi udindo wolemekeza lamulo loletsali.

*Choncho,* titapanga malonjezano amenewa, ife mwaife tokha eni komanso zipani zathu zandale ngakhale otiiimilira kapena wina aliyense wolowa mmalo mwathu sadzachita zinthu zofuna kunyazitsa komanso kuderera mphamvu za bungwe loyendetsa zisankho. Mwa ichi, ife tidzagwirizana kwathunthu ndi bungwe loyendetsa zisankho mu ntchito zake zonse ndipo ife tidzachita zinthu zowonetsetsa kuti chisankho chichitike mopambana ndipo sitidzachita zinthu zomwe zingasokoneze kayendetsedwe ka chisankho.

Talonjeza izi lero pa 19 March 2019

Ku Lilongwe

1. Grace Chupa………………………………………………………………………
   Mlembi wamkulu, Alliance for Democracy (AFORD)

2. Greydon Mikuwa……………………………………………………………………
   Mlembi wamkulu, Democratic Federal Alliance (DFA)

3. Nelson Nyirenda……………………………………………………………………
   Mlembi wamkulu, Democratic People Congress (DEPECO)

4. Grelzedar Jeffrey……………………………………………………………………
   Mlembi wamkulu, Democratic Progressive Party (DPP)

5. Steven Njobvuyalema…………………………………………………………………
   Mlembi wamkulu, Freedom Party (FP)

6. Mabvuto Alfred Ng'ona..................................................................................

   Woima Payekha pa chisankho cha President Reverend Hadwick Kaliya

7. Eisenhower Mkaka..........................................................................................

   Mlembi wamkulu, Malawi Congress Party (MCP)

8. Sam Banda.....................................................................................................

   Mlembi wamkulu, Mbakuwaku Movement for Development (MMD)

9. Brian Sunduza Phiri.........................................................................................

   Mlembi wamkulu, National Salvation Front (NASAF)

10. Ibrahim Matola..............................................................................................

    Mlembi wamkulu, Peoples Party (PP)

11. Aubrey Nkata.................................................................................................

    Mlembi wamkulu, Peoples Transformation Alliance (PETRA)

12. Grant Chimenya.............................................................................................

    Mlembi wamkulu, Tikonze Peoples Movement (TPM)

13. Bright Msusku................................................................................................

Mlembi wamkulu, Umodzi Party (UP)

14. Kandi Padambo…………………………………………………………………………………

Mlembi wamkulu, United Democratic Front (UDF)

15. Patricia Kaliati………………………………………………………………………………..

Mlembi wamkulu, UTM

Tatsindika izi ku Lilongwe leo pa 19 March 2019 pamaso pa

…………………………………………………………………………………………………………

………………………

Justice Dr Jane Ansah SC, JA

**M'khala pampando wa Bungwe Loyendetsa Zisankho m'Malawi**